



**AFRICA MUSLIMS AGENCY
KUWAIT**

**MALAMULO A KUSALA
MCHISILAMU**

**OFUFUZA NDI KUTANTHAUZIRA:
OFFICE YA {A.M.A}
MALAWI**



*Africa Muslims Agency
Kuwait*

Bukuli Ndi Lawulere

**MALAMULO A KUSALA
MCHISILAMU**

**OFUFUZA NDI KUTANTHAUZIRA:
OFFICE YA {A.M.A}
MALAWI**

www.islamic-invitation.com

LIKUPEREKEDWA ULELE NDI:

*Africa Muslims Agency
P.O.Box 1632, Lilongwe
MALAWI*

أحكام الصيام في الإسلام - لغة شيشيوا

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ

Mu Dzina La Mulungu Mwini chifundo
Chambiri Mwini chisoni

1: Tanthauzo:- (تعريف الصيام)

Kusala ndiye kuti kusiya, monga m'mene ziliri apa:-
"Ndithu ine ndapereka pangano kwa Mulungu loti ndisale.
Choncho sindilankhula ndi wina aliyense lero." (26: مريم)
(Suratu Maryam 26)." Liwu la kusala apa likutanthauza
kuti kusiya kulankhula. Ndiye kusala tanthauzo lake ndi
kusiya kuchita chinthu chilichonsecho kulankhula nga-
khale kuchita. Koma m'malamulo a chisilamu liwuli
limatanthauza kuti:- Kusiya kudya, kumwa, kukhala malo
ndi mkazi, osanena mawu opanda pache, kupanga tchimo
ndi kunena mawu oletsedwa ndi zina zonse zomwe
chisilamu chaletsa kuyambira kutuluka kwa FAJR
(m'banda kucha) mpaka kulowa kwa dzuwa. Zonsezi ziri
m'mawu a Mulungu ndi Mtumiki wake awa:-

Mulungu akuti:- "Ndipo idyani, imwani mpaka muthe
kusiyantsa pakati pa ulusi oyera ndi wakuda [umenewo ndiye
m'banda kucha,] kenako pitirizani kusala mpaka madzulo
(AL- BAQARA: 187)." (البقرة: 187)

Hadith:- "Amene sasiya kunena mawu onyansa oletsedwa
ndi kupanga za machimo ndi mtopola, Mulungu alibe nazo
kanthu za kusiya kwake chakudya ndi zakumwa zake,"
anailandira AL- BUKHARIYY ndi ABOU DAWOOD.

2: UMBONI WA KUSALA:- (دليل مشروعية الصيام)

Lamulo la kusala linasindikizidwa ndi Qur'an, Hadith

ndi kugwirizana (mosasemphana zonena) kwa anthu odziwa ophunzira.

1- Mulungu wanena kuti:- "E! Inu anthu okhulupilira mwalamulidwa kuti mudzisala chimodzi-modzi ndi m'mene analamulidwira anthu akale chifukwa choti mukhale anthu owopa iye Mulungu, kusalako ndi masiku owerengeka, ndiye amene angapezeke kuti akudwala kapena ali pa ulendo (wa 70 km kumapitilira) angathe kumasula ndi kudzabweza pa nthawi ina masikuwo ndipo anthu amene kukuwabvuta kusalako ayenera kupereka m'malo mwake chakudya kwa anthu obvutika, ndipo amene adzipereke pa zabwino ndiye izo nzabwino kwa mwini wacheyo, koma kusala ndi kumene kuli bwino zedi kwa inu, mukadakhala kuti mukudziwa. Mwezi wa Ramadhwan ndi umene Qur'an inatsitsidwa kuti ikhale chinthu choongolera anthu ku zabwino ndiponso kuti ikhale ngati dongosolo la njira yowongoka ndi kusiyantsa zabwino ndi zoipa. Ndiye amene angawone mwa inu mweziwo ayenera kusala. (AL-BAQBARA: 183-187)

2- Adanena ABDULLAH bin UMAR (R.A) kuti:- "Mneneri wa Mulungu anati:- "Chisilamu chamangidwa pa nsanamira zisanu:- Kutsimikiza ndi kuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma Mulungu m'modzi yekha basi ndipo Muhammad ndi mthenga wa Mulungu. Kupemphera kasanu pa tsiku (swalaah), ku-

pereka chiyeretso cha chuma kamodzi pa chaka (zakaah) kupita ku Hajj (Mecca) ndi kusala m'mwezi wa Ramadhwan." (anailandira mofanana AL-BUKHARIYY ndi MUSLIM)

3- Anthu onse a mpingo wa Chisilamu palibe ndi m'modzi yemwe amene anatsutsana nazo zoti kusala ndi lamulo lokakamidwa kwa onse a mpingowu, ndikuti kusala ndi imodzi mu nsanamira za Chisilamu.

3: Zolinga za kusala (Kumanga) **حكمة الصيام**

Abale anga olemekeza zindikirani kuti Chauta adatilamula ife malamulo osiyana-siyana ndiponso ndi zolinga zake, ndipo zina mwa zolinga za malamulo amenewa adatifotokozera, mwa chitsanzo kumanga m'mwezi wa Ramadhwan. Choncho tiyeni tione kuti cholinga cha lamulori ndi chiyani:-

(01) Cholinga chapamwamba -mwamba cha kusala ndi chomwe iye (Mulungu) wa pamwambamwamba watiuza mu bukhu lolemekezeke la Qur'an kuti:-

"E! Inu anthu amene mwakhulupilira (mwa Mulungu ndi atumiki ake) kwalamulidwa kwa inu kumanga (mwezi wa Ramadhwan) monga momwe adalamulidwiranso anthu ena inu musadabwere cholinga chake ndi choti mukhale anthu owopa Mulungu"

(02) Kumanga (kusala) ndi chinsinsi cha pakati pa munthu ndi Chauta wake, chifukwa pali malamulo ena omwe munthu amawatsata ndi kumawachita pa gulu la

wanthu pomwe kumanga munthu amakhala ndi ufulu oti atha kudya kapena kumwa pa iye yekha koma chifukwa choti mtima wake uli odzadzidwa ndi mantha ndiponso manyazi ndi Mulungu zonsezi amasiya kuzichita.

- (03)(i) Kuuzoloweza mtima ndi ziwalo zonse zamthupi kukhala zogonjera m, malamulo a Chauta.
- (ii) Kusala kumakhala sukulu (maphunziro) kwa munthu pakumuphunzitsa kukhala oleza mtima komanso wa chifundo ndi anthu amnzake.
- (iii) Kumuphunzitsa kukhala munthu owolowa manja pa kupereka.

4: OKANIRA LAMULOLI:-

(حكم من أنكر فرضية الصيام)

Chifukwa cha maumboni onsewa, amene angatsutse lamulo la kusala m'mweziwu ndiye kuti akhala kunjwa kwa mpingowu (kafir) chifukwa chotsutsa lamulo lodziwika ndi ma umboni okwanira mosakaikitsa, ndi kukanira kwake mawu omveka a Qur'an ndi Hadith ya pamwambamwamba.

5: NTHAWI YOMWE LIDATSIKA LAMULOLI:-

(تاريخ فرضية الصيام)

Mulungu analamula Asilamu za kusalaku m'chaka chachiwiri chisamukire ku Mecca, mwakuti Mtumiki wa

Mulungu (SAW) pamene ankamwalira anali atasala Ramadhwan zisanu ndi zinayi. Ndipo lamuloli linatsika patangotsala masiku awiri okha a mwezi wa SHA'ABAN [womwe umati ukatha ndikumabwera mwezi wa RAMADHWAN.]

6: UBWINO WA KUSALA:- (فضل الصيام)

Ma umboni onena ubwino wa kusala mmawu a Mtumiki ndi ambiri osawerengeka. Tingotenga ma umboni ochepa okha mmalo mwa chitsanzo:-

- 1- **Abou Huraira anati:-** "Mtumiki wa Mulungu ananena kuti:- Mulungu akunena kuti:- Ntchito zonse za mwana wa Adam ndi zache kupatula kusala, zimenezo ndi za ine ndipo ine ndi amene ndilipire zimenezo. Ndipo kusala ndi chishango, ndiye wina mwa inu akasala asanene zoipa ndipo asakweze mau popanda pache, tsono ngati wina wamutukwana kapena kummenya angoti:- Ndithu ine ndasala, ine ndasala, ndikumulumbilira amene moyo wa Muhammad uli m'manja mwake, fungo lomwe limatuluka mkamwa mwa osala ndi lonunkhira zedi kwa Mulungu kuposa fungo la mafuta onunkhira, osala ali ndi kusangalala kuwiri kumene asangalale. Pomasula amasangalala ndi kumasulako, ndipo akadzakumana ndi mbuye wake adzasangalala ndi kusala kwake." Al-Bukhariy, Muslim, AL-Nasa-Iyy.
- 2- **Abou- Huraira ananena kuti:-** "Mtumiki wa Mulungu ada-

ti:- Pitani ku nkondo mukapeza kanthu, salani mukhala a ngwiwo ndipo yendani-yendani mulemera"] AL Twabara-Niyy.

3- Iyenso adati:- Pamene unadza mwezi wa Ramadhwan- Mtu-miki wa Mulungu anati:- "Ndithu wakufikirani mwezi wa madalitso womwe Mulungu anakulamulani kusala mmene-mu zimatsegulidwa zitseko za ku mtendere ndi kutsekedwa zitseko za ku moto, ndipo a satana amaikidwa mitengo mkhosi mwao, mmenemu muli usiku umodzi womwe uli ndi zabwino zambiri kuposa zomwe mungachite pa miyezi chikwi chimodzi (1,000), amene amanidwe zabwinozi ndiye kuti wamanidwa zedi."

4- Mtumiki wa Mulungu adati:-

Ukabwera mwezi wa Ramadhwan zimatsekulidwa zitseko za kumalo a mtendere- ndipo satana amamangidwa ndiponso amaitana oitana kuti:- Iwe amene ukufuna zabwino bwera, iwe amene ukufuna zoipa lekera pommwepa, ndipo Mulungu ali ndi anthu amene amawachotsa ku moto, ndipo zimenezi zimachitika usiku uliwonse mpaka Ramadhwan ithe."

M'bale wanga msilamu! Dziwa kuti Mulungu analamula kuti tizisala, ndipo kusala ndi kumvera Mulungu ndipo kuli ndi phindu lake monga:-

1- Kusala kumapangitsa kuti m'mimba mupume pa ntchito yake yolemetsa yosadukizayo, ndi kusungunula zotsala ndi kulimbisa ndipo ndi kothandiza zedi pa matenda ambiri,

chinanso kumapatsa mpata wabwino kwa osuta fodya wo-siyira kusutako ndi kuwathandidza kusiya kusuta.

- 2- Kusala kumayeretsa mtima kumauzolowetsa kuchita zabwino ndi mndandanda, kumvera, kupilira ndi kuzi-pereka.
- 3- Osala amamva mu mtima mwake kuti ndi ofanana ndi amnzake osala, ndiye amasala nawo ndi kumasula li-modzi, ndipo amamva mu mtima mwake umodzi wa Chisilamu, ndi kumva njala ndikumathandiza amnzake a njala ndi osauka.

(7) MITUNDU YA KUSALA:- (أنواع الصيام)

MTUNDU OYAMBA:- (النوع الأول)

Kusala kokakamizidwa... Ndipo pali magulu awiri:-

(A) KUSALA MU NTHAWI YODZIWIKA POYAM-BIRA NDI POTHERA.

(الصيام المعلوم زمن ابتدائه وانتهائه)

- (1) Imeneyo ndi Ramadhwan chifukwa cha mau a Mulungu oti:- "Aliyense amene angauwone mwezi [wa Ramadhwan wa mu mpingo wanu] amange."
- (2) Kupereka pangano kwa Mulungu loti ndidzasala nthawi yakuti-yakuti chifukwa cha mau a Mulungu oti:- "NDIPO AYENERA KUKWANITSA PANGANO LAWO." Ndi mau a Mtumiki (SAW) oti:- Amene aper-eke pangano kwa Mulungu loti amumvera ayenera ku-

panga chimenecho, ndipo amene alonjeze zoti amunyoze asamunyoze AL- BUKHARIYY ndi MUSLIM.

B- KUSALA KOKAKAMIZA KOPANDA NTHAWI YENI-YENI:

(الصيام الواجب غير المخصوص بزمن)

Kumeneko ndi kusala mobweza masiku amene anamasula mu Ramadhwan chifukwa cha ulendo kapena kudwala kapena china chotero monga kudwala pa mwezi uliwonse kwa mzimayi ndi kudwala kwake akangobereka kumene, umboni wake ndi uwu:- "Ndiye amene apezeke mwa inu kuti akudwala kapena ali pa ulendo ndi kumasula azabweze masikuwo m'miyezi ina." Hadith imene Aisha (R.A) akunena kuti:- Tinali kudwala matenda athu a chizimayi nthawi ya Mtumiki (SAW) ndiye timalamulidwa kuti timasule ndipo tibweze masiku amene tamasulawo, koma sitinkalamulidwa kuti tibweze mapemphero amene tawasiya chifukwa cha matendawo." AL- Bukhariyy ndi Muslim

MTUNDU WACHIWIRI:- (النوع الثاني)

KUSALA MWA KUKONDA KWAKO

(الصيام المستحب)

Kumeneko ndi kusala kumene Mtumiki wathu Muhammad (SAW) anauza anthu ubwino wa kusalaku, ndipo kuli ndi zigawo ziwiri:-

A- KUSALA MU NTHAWI YAKE-YAKE MONGA:-

(الصيام المخصوص بزمن)

Kusala masiku asanu ndi limodzi mmwezi wa SHAW-WAL [womwe uli pambuyo pa mwezi wa Ramadhwan] umboni wake ndi uwu:- "Mtumiki (SAW) ananena kuti:- "Amene asale mmwezi wa Ramadhwan ndi kusalanso masiku asanu ndi limodzi a mwezi wa Shawwal akhala ngati wasala chaka chatunthu." MUSLIM NDI ENA.

B- Kusala tsilu la ARAFAH (kwa amene sali ku Hajj):- Umboni wake ndi mau a Mtumiki awa:- "Kusala tsiku la ARAFA kumafafaniza machimo a zaka ziwiri chaka chatha ndi chaka chikudza, tsono kusala tsiku la khumi mmwezi wa MUHARRAM. Kumafafaniza matchimo a chaka chatha chonse." MUSLIM NDI ENA KUPATULA AL-BUKHARIYY NDI AL-TIRMIDHIYY.

C- KUSALA PA TSIKU LA KHUMI M'MWEZI WA MUHARAM:- (صيام العاشر من محرم)

Umboni wake ndi mawu a Mtumiki awa:- "Ndithu ili ndi tsiku la khumi [mwezi wa MUHARRAM, koma simukukakamidwa kusala - koma ine ndasala - tsono amene akufuna asale, ndipo amene sakufuna asasale." AL-BUKHARIYY NDI MUSLIM.

Ndipo nkhani yachokera kwa mwana wa ABBAS (R.A) yoti:- "(Mtumiki wa Mulungu (SAW) anafika ku Medina

ndipo anawapeza Ayuda akusala tsiku la khumi (mmwezi wa MUHARAM) ndiye anafunsa kuti:- Kodi ndi tsiku lanji limeneli? Adayankha kuti:- Iri ndi tsiku labwino lomwe Mulungu adampulumutsa Musa ndi ana a Israeli (AYUDA) kwa adani awo, ndiye Musa anali kusala tsikuli. Mtumiki (SAW) anati:- Ine ndi amene ndiri oyenera kutsata za Musa kuposa inu." AL-BUKHARIYY NDI MUSLIM.

Adanenanso Mtumikiyo kuti:- "Ngati ndikhale moyo mpaka chaka cha mawa nidzasala tsiku la chisanu ndi chinayi (9)." Muslim.

D- (صيام العشر الأوائل من ذي الحجة) Kusala masiku khumi oyamba a mwezi wa DHIL-HIJJA, umboni wake ndi mau a Hafswa (R.A) oti:- "Pali zinthu zinayi zomwe Mtumiki (SAW) sanali kuzisiya:- Kusala tsiku la khumi mmwezi wa DHIL-HIJJA, kusala masiku atatu mmwezi uliwonse ndi kupemphera ma Rak'ah awiri isanakwane nthawi ya usana."

Tsono masiku khumiwa osawerengera la khumili ayi chifukwa ndi tsiku la Eid .Koma kusiira pa" 9".

E:- KUSALA TSIKU LOLEMBA NDI LACHINAYI:-

(صيام الإثنين والخميس)

Umboni wake ndi Hadith yomwe adailandira Abou Huraira (R.A) yoti:- " Mtumiki (SAW) anali kusala kawiri-kawiri tsiku lolemba ndi la chinayi ndiye atafunsidwa iye anati:- Ndithu ntchito za munthu zimakaonetsedwa kwa

Mulungu tsiku lolemba ndi lachinayi, ndiye Mulungu amamukhulukira msilamu aliyense ndi okhulupilira aliyense kupatula anthu onyanyalana (okwiyirana) iye amati:- Asiyeni kaye" AHMAD.

MTUNDU WACHITATU:- (النوع الثالث)

KUSALA KOPANDA NTHAWI YENI-YENI MONGA:

(صيام غير المخصوص بزمن)

1- Kuchulukitsa kusala mmwezi wa SHA'ABAN chifukwa cha Hadith ya Aisha yoti:- Sindinamuone Mtumiki (SAW) akusala mwezi watunthu pokha-pokha mwezi wa RAMADHWAN, ndipo sindinamuone akusala masiku ambiri a miyezi ina kuposa mwezi wa Sha'aban."

2: KUSALA MASIKU OCHEPA A MIYEZI YOLEMEKEZEKA INAYI (4):-

(صيام بعض أيام الأشهر الحرم)

Chifukwa cha mawu a Mtumiki kwa munthu wina oti:- "Uzisala masiku owerengeka a miyezi yolemekezeka kenako nkusiya." Ndiye ankasonyeza zala zake zitatu. (AL-BUKHARIYY NDI MUSLIM).

3- KUSALA MASIKU ATATU PA MWEZI:-

(صيام ثلاثة أيام من كل شهر)

Chifukwa cha Hadith ya Abie Dharri AL- Ghifariyy (R.A) yoti:- Mtumiki wa Mulungu (SAW) anatilamula

kuti tizisala pa mwezi uliwonse masiku atatu oyera:- Pa 13,14, 15 ndipo anati:- Kusala masiku amenewa kuli ngati kusala chaka chatunthu." AHMAD, ABOU DAUD, IBNU MAJA NDI BAIHAQIYY Apa tiyenera kudziwa kuti madeti omenewa osati amyezi ya chizungu ai, koma amyezi ya chisilamu omwe deti "1" imayamba tsiku lomwe waoneka mweziwo

4- KUSALA TSIKU NDI KULEKA TSIKU LINA:-

Chifukwa cha mau a Mtumiki (SAW) oti:- "Kusala kokonedwa kwa Mulungu ndi kusala kwa Dawood, ndipo pemphero lokonedwa kwa Mulungu ndi pemphero la Dawood, anali kugona theka ya usiku ndi kupemphera 1/3 yake ndi kugona 1/6, ndipo anali kusala tsiku ndi kumasula tsiku linalo." IBNU HIBBAN NDI INNASA IYY.

KUSALA KOLETSEDWA: (الصيام المنهي عنه)

1- Kusala tsiku la Eid chifukwa Abou Saeed anati:- "Mthenga wa Mulungu (SAW) analetsa kusala masiku awiri:- Tsiku lomasula ndi tsiku lozinga." L- BUKHAR-IYY, MUSLIMS.

2- Kusala kwa mayi odwala matenda ache a pamwezi: ndi a pambuyo pa kubeleka (صيام الحائض والنساء)

Chifukwa Aisha anati:- "Tinali kudwala nthawi ya Mtumiki (SAW) matenda athu a pamwezi, ndiye tinali kulamulidwa kuti tibweze masiku amene tamasulawo, koma sitimalamulidwa kubweza mapemphero (Swalaah)."

Moti amenewa akanati asale pamene matendawo asanathe sizikanalodedwa ndipo akadayenera kubweza.

3- KUSALA MASIKU A PAMBUYO PA EID YA ADH- HA

(صيام أيام التشريق)

Mtumiki (SAW) anati:- "Masiku (atatu)a pambuyo pa tsiku la Eid il-adh-ha ndi masiku a kudya ndi kumwa ndi kutchula Mulungu wamphamvu, wolemekezeka." Muslim.

4- KUSALA KWA MAYI MWAKUKONDA KWAKE PAMENE MWAMUNA WAKE ALIPO MOPANDA CHILOLEZO CHAKE

5- KUSALA TSIKU LA ARAFA (KWA WA HAJJ):-

(صيام يوم عرفة للحاج)

Chifukwa pali Hadith yochokera kwa Abie Huraira yoti:- "Mtumiki wa Mulungu (SAW) analetsa kusala tsiku la Arafa ku Arafa, ndipo ena ananena kuti Mtumiki (SAW) sanasale tsiku la Arafa pamene iye anali ku Arafako."

6- KUSALA TSIKU LA CHISANU LOKHA:-

(تخصيص يوم الجمعة بالصوم)

Umboni wake ndi Hadith ya Abie Huraira (R.A) yoti:- Mtumiki wa Mulungu anati:- "Asamange wina aliyense mwa inu tsiku lachisanu, koma azikhala kuti anayamba dzulo lake kapena asalenso mawa lake"

7- KUSALA CHAKA CHATUNTHU:- (صيام الدهر)

Umboni wake ndi Hadith iyi "SANGALANDIRIDWE

AMENE WASALA MOSADUKIZA CHAKA CHATUNTHU" mu Hadith ya Abie QATADA "SAPEZA MALIPIRO A KUSALA NDIPO IYE SAKUDYA" MUSLIM.

8- KUSALA MOPANDA KUMASULA MADZULO:-

(الوصال في الصيام)

Umboni wake Hadith ya Abie Huraira (R.A) yoti:- "Mtumiki (SAW) analetsa kusala mosalekeza, ndiye munthu wina mwa Asilamu anati:- Inuyo Mtumiki (SAW) simulekeza, iye anati:- Nanga ndi ndani mwa inu amene angafanane ndi ine? Inetu ndimati ndikagona ndimadyet-sedwa ndi kumwetsedwa ndi bwana wanga." Tsono pamene anthu aja anakana zosiya kulumikiza kumanga Mtumiki anapitiriza nawo tsiku limodzi ndi tsiku linalo kenako anawuona mwezi wa RAMADHWAN, ndiye anati:- "Ukanati uchedwe mweziwu kuwoneka ndikanapitiriza nanu." Kunali ngati kuwakhaulitsa pamene anakana.

KODI KUSALA MWEZI WA RAMADHWAN KUMATSIMIKIZIKA NDI CHIANYI?

(بم يثبت صيام رمضان)

Kusala kumatsimikizika ndi nsanamira izi:-

- 1- Kuwoneka mwezi wa Ramadhwan:- Kuwona ndi maso kapena kukwana masiku makumi atatu a mwezi wa Sha'aban, chifukwa Mtumiki (SAW) anati:- "Salani chifukwa chowona mweziwo ndipo masulani chifukwa

chouwona, tsono ngati wabisika m'mitambo mungowerengera masiku makumi atatu a mwezi wa Sha'aban." AL- BUKHARIYY NDI MUSLIM. Kuuwona mweziwo munthu m'modzi wodalilika, wosakaikitsa pa makhalidwe ache ndi zobvomerezeka, ngati sanaoneke woteroyo ndiye kungowerengera masiku makumi atatu a Sha'aban ndi kuyamba kusala tsiku linalo.

Koma mwezi wa Shawwal uyenera kutsimikizika pokhapokha atakwana masiku makumi atatu a Ramadhwan kapena kuwuona anthu awiri a makhalidwe awo a pamwamba ngati zabvuta kuonekako.

2- CHITSIMIKIZO CHA KUSALA: (نية الصيام)

Tanthauzo lake ndi loti kukhala ndi cholinga cha kusala. Ndipo malo a chitsimikizo ndi mumtima, ndipo chimatsimikizika ndi chirichonse chosonyeza kusala ngakhale ndi DAKWI kapena kutsimikiza kuti aleka zomasulitsa kusala. Nthawi yopangira chitsimikizochi ndi kuyambira kulowa kwa dzuwa malire kutuluka kwa Fajr (mlenga ng'amba/chichinga usiku(m'banda kucha) . Mtumiki (SAW) adanena kuti:- "Amene asiye kupanga chitsimikizo usiku ndiye kuti kusala kwake sikulandilidwa."

3- KUSIYA KUPANGA ZONSE ZOMASULITSA:

(ترك جميع المفطرات)

Kuyambira ku mlera ng'amba mpaka kulowa kwa dzuwa, chifukwa cha mau a Mulungu awa:- "Idyani imwani mpaka ukuonekereni ulusi woyera ndi wakuda

mlera ng'amba kenako mupitirize kusala mpaka usiku"
AL-BAQARA:187.

Ndipo kusalako sikungakhale kokwanira ndi kugwirizana ndi malamulo a kusala mpaka atasiya chibwana ndi mau onyansa ndi mau oletsedwa ndi oipa, chifukwa Mtumiki analetsa zonsezo pa kusala mowonjezera zedi kuposa masiku ena onse, m'mahadith imodzi yake ndi iyi:- "Kusala sikusiya kudya ndi kumwa kokha ai, koma kusala kweni-kweni ndi kusiya chibwana ndi mau oipa."

MAGULU A WANTHU PA KUSALA:

1- AMENE ALI OKAKAMIZIDWA KUSALA NDIPO SAKULOLEDWA KUMASULA:

Anthu amenewa ndi awa:- Msilamu aliyense amene sali wamisala, ndipo ndi wokwana msinkhu, sakudwala, wakutha kusalako, sali pa ulendo. Ngati ali wamkazi ayenera kukhala wosadwala matenda a pa mwezi kapena matenda amene amadza atangobeleva kumene . Akakhala kutali ndi zonsezi ayenera kusala ngati enawo ndipo aliyense mwa iwowa ngati amasule lamulo lawo likhala motere:-

A- Ngati amasule moiwala, ndiye kuti sapeza machimo ndipo asadzabweze tsikulo ngakhale kufafaniza ndipo kusala kwawoko ndi kobvomerezeka, umboni wake ndi mau a Mtumiki (SAW) oti:- "Amene waiwala kuti wasala ndi kudya kapena kumwa, akakumbukira alekeze ndipo

apitirize kusalako chifukwa wamudyetsa ndi kum'mwetsa ndi Mulungu."

Hadith ina yachokera kwa ABIE HURAIRA ndi kuilandira AL-HAKIM ikuti Mtumiki wa Mulungu (SAW) anati:- Amene wamasula mwezi wa RAMADHWAN moiwala saku-kakamizidwa kubweza ngakhale kufafaniza. "

B- KUMASULA MWADALA PAKUKHALA MALO NDI MKAZI

Ndiye ameneyo ayenera kubweza tsiku limeneri ndipo ayeneranso kufafaniza. Umboni wake ndi Hadith ya Mtumiki (SAW) yomwe anailandira Abou Huraira (R.A) yoti: Anabwera munthu kwa Mtumiki (SAW) ndiye anati:- Ndawonongeka! Mtumiki anati:- Chakuononga nchiani? Anati:- Ndakhudzana ndi mkazi wanga masana a mwezi wa Ramadhwani. Mtumiki anati:- Kodi uli ndi kapolo woti ndikumpatsa ufulu? Munthu uja anati:- Ayi. Mtumiki anati:- Nanga uli ndi chakudya choti mkuwapatsa obvutika okwana makumi asanu ndi limodzi (60)? Anati ayi. Kenako munthu uja anakhala pansu. Ndiye wina anabweretsa kwa Mtumikiko thumba la tende, [mtundu wina wake wa zipatso] ndiye Mtumiki anampatsa munthu uja ndi kumuuzza kuti:- Uwapatse anthu obvutika zimenezi. Munthu uja anati:- Kumpatsa obvutika kuposa ife? Palibe m'Madina muno banja loyenera kulandira zimenezi kupo-

sa ife. Mtumiki (SAW) anaseka mpaka zigama zinaonekera, kenako anati:- Pita ukapatse banja lako.

C- Kumasula dala-dala pakudya kapena kumwa ndi zina zotero. Iwo amene achite zimenezi ayenera kubweza tsiku limeneli, komabe apeza machimo omwe ngakhale atasala chaka chatunthu sangakhulukidwe chifukwa cha mau a Mtumiki (SAW) oti:- "Amene wamasula dala tsiku limodzi la mwezi wa RAMADHWAN popanda chifukwa chobvomerezeka (Mchisilamu) sizingafafanitsidwe ndi kusala kwa chaka chatunthu ngakhale atasala chaka."

2- AMENE AFIKA POKAKAMIZIDWA KUSALA KOMA AKULOLEDWA KUMASULA NDI KUKAKAMIZIDWA KUPEREKA KANTHU M'MALO MWACHE:

Amenewa ndi anthu okalamba zedi mkazi ngakhale mwamuna ndi wodwala amene sizikudziwika kuti achira, mgululi akulowamo anthu ogwira ntchito zolemetsa kwam-biri ndipo sapeza zofunikira pa moyo wawo mokwanira koma zokhazo zimene amachitazo basi. Akulowamonso mzimayi wa pakati ndi woyamwitsa ngati akuopa kuti kusalako kumpatsa mabvuto iye kapena mwana wake. Amenewa ayenera kupereka chakudya kwa obvutika tsiku ndi tsiku chokwanira (750 g)

3- AMENE AFIKA POKAKAMIZIDWA KUSALA KOMA AKULOLEDWA KUMASULA NDIPO AKUKAKAMIZIDWA KUBWEZA:

Amenewa ndi anthu odwala kapena a paulendo (woyambira pa 70 KM kumapitilira) chifukwa Mulungu wanena kuti:- "Ndipo amene adwale kapena kukhala ndi ulendo atha kumasula ndi kubweza masikuwo pa nthawi ina." Koma kuti chabwino n'chiti:- Kusala kapena kumasula? Kapena chomwe angathe kupangacho kapena chomwe chingampekure? Zonsezi anthu ananena, choncho munthu asankhe molingana ndi chibadwa.

4- AMENE AFIKA POKAKAMIZIDWA KUMASULA NDI KUBWEZA KOMWE:

Iwowa ndi mzimayi yemwe akudwala matenda ake achizimayi a pamwezi ndi amene akudwala matenda a chizimayi omwe amayamba chifukwa cha kubereka. Onsewa ayenera kumasula, ndipo sakulolelwa kusala chifukwa akatero sizibvomerezeka kwa Mulungu, koma akadzathana nawo mabvutowa adzabweze masiku aja anamasula, umboni wa zimenezi tautchula kale m'mbuyomu.

5- AMENE SANAFIKE POKAKAMIZIDWA KOMA AKUNGOLAMULIDWA KUSALAKO KUTI AZOLWERE:

Ameneyu ndi mwana yemwe wakula koma sanafike podziloteru, chifukwa aliyense amene sanathe msinkhu ndiye kuti sakuwumirizidwa kanthu kena kalikonse m'Chisilamu, umboni wake ndi mau a Mtumiki (SAW) oti:- "Pali anthu atatu amene salembedwa zabwino ngakhale zoipa:- Wamtulo mpaka adzuke

kaye, wamisala mpaka idzathe, ndi mwana mpaka adzayambe kuziloteru."

Tsono kufunsidwa kwa omuyang'anira kuti azimulamula kuti asale nchifukwa cha Hadith yomwe anailandira AL-RUBAYYI- I-BINTU MUAWWIDH (R.A) kuti:- "Mtumiki (SAW) anatuma munthu ku mzika za ku Madina tsiku la khumi m'mwezi wa MUHARRAM kuti akauze zoti:- Amene wadzuka lero, atasala apitirize kusalako, ndipo amene wadzuka osasala asale nthawi yatsalayi, ndiye tinali kusala tsiku limeneli ndi kumalamula ana athu kuti asale, ndikumapita ku Mzikiti ndi kumapatsa anawo choseweretsa chathonje, ndipo wina akalilira chakudya timampatsa chakudyacho, timapanga zimenezi mpaka ikwane nthawi yomasula."

ZINTHU ZOWONONGA KUSALA: (مبطلات الصيام)

Zomwe zitchulidwe apa ndi zinthu zowononga kusala ngati wina atachita chimodzi mwa zinthuzi:-

- 1- Kudya kapena kumwa dala-dala.
- 2- Kusanza dala chifukwa cha Hadith iyi:- "Ndipo amene wasanza mwadala ayenera kubweza tsikulo."
- 3- Kudwala ku mwezi ndi matenda oyamba atangobala kumene ngakhale zimenezo zitachitika dzuwa litangotsala pang'ono kulowa.
- 4- Kutuluka kanthu ku maliseche ake chifukwa chopsopsona mkazi wake kapena kumukumbatira kapena kuseweretsa

ndi mkono wake, zimenezi zimaononga kusala ndipo munthuyo ayenera kubweza tsiku limeneli.

- 5- Kukhudza mkazi (kupanga naye ukwati) ndipo chokhachi ndi chimene munthu ayenera kubweza tsikulo ndipo adzapange chinthu chofafanizira tchimo lakumasula pa chifukwa chimenechi. Kufafanizako ndi kupanga chimodzi mwa izi:-
 - A- Kumpatsa kapolo ufulu.
 - B- Ngati ulibe usale miyezi iwiri mondondoza, ngati wadukiza. Popanda chifukwa mu zifukwa zomasulira zija ayam-birenso.
 - C- Ngati sutha kutero upereke chakudya kwa obvutika okwana (60) makumi asanu ndi limodzi. Palibe kusiyana pakati pa mkazi ndi mwamuna.
- 6- Kutuluka mchisilamu. Umboni wake ndi mau a Mulungu awa:- "Ndithu ukangomusanganiza Mulungu ndi china chake ntchito yako yonse iwonongeka." AL-ZUMAR:65
- 7- Kutsimikiza kuti ndimasule ndi kukaika-kaika za kusalako. Zimenezinso ndi zomasulisa.
- 8- Kulowetsa dala kanthu kukhosi kapena mu ubongo wake, koma jakisoni ya mankhwala ndiye siononga ai koma yokhutitsa ndiye yoonongetsa.

ZINTHU ZOSAWONONGA KUSALA: (ما لا يبطل الصيام)

- 1- Kudzithira madzi ngakhale kubiramo, chifukwa cha Hadith yoti:- "Mtumiki (SAW) anali kuthira madzi pa

mutu wake pamene iye anali atasala, ankapanga zimenezi chifukwa cha ludzu ndi kutentha."

- 2- Kugwiritsa ntchito mankhwala okongoletsa maso kape-na kuchiritsira. Umboni wake ndi Hadith imene anailandira Anasi (R.A) kuti:- "Mtumiki (SAW) anali kukongoletsa maso ake pamene iye atasala."
- 3- Kupsopsona (kwa amene angathe kuugwira mtima wake). Aisha (R.A) anati:- "Mtumiki (SAW) anali kupsopsona atasala ndi kukumbatira atasala, koma anali owugwira mtima."
- 4- Kutsuka mkamwa ndi m'mphuno mosapitilira muyezo chifukwa Mtumiki (SAW) anati:- "Ukamatsuka mkamwa udzitsuka mokwanitsa bwino, kupatula utasala."
- 5- KULUMIKA:- Chifukwa Mtumiki (SAW) analumika pamene iye atasala.
- 6- KUNUNKHIZA:- Apa tikunena chinthu china chirichonse chomwe chiri ndi fungo labwino. Palibe umboni oletsa kununkhiza ngakhale muli mu Ramadhwan. Choncho palibe kanthu kununkhiza fungo lonunkhira ngakhale utasala, ngakhale loipa .

ZABWINO KUPANGA UKASALA:

- 1- Kudya dakwi: kumeneko ndi kudya kapena kumwa chirichonse ngakhale madzi okha, ndipo nthawi yake kuyambira pakati pa usiku malire kutuluka kwa "Faj-ri"mlenga ng'amba, [m'banda kucha] ndipo Mtumiki

(SAW) anati:- "Idyani dakwi chifukwa m'menemo muli madalitso."

- 2- Osachedwetsa kumasula nthawi itakwana. Chifukwa Mtumiki (SAW) anati:- "Anthu sangaleke kukhala ndi zabwino ngati akumasula mosachedwetsa."
- 3- Kulimbikira mapemphero m'masiku khumi omaliza a mwezi wa Ramadhwan. Pali Hadith yomwe adailandira Aisha (R.A) yoti:- "Mtumiki (SAW) amati akafika masiku khumi omaliza a mwezi wa Ramadhwan amadzukira usiku mapemphero ndipo amadzutsa akazi awo ndipo amamanga molimba bwino nsalu." [sanali kukhala nawo malo m'masiku khumi onsewa.]
- 4- Kutsuka mkamwa. Chifukwa Mtumiki (SAW) anali kutsuka mkamwa akasala.
- 5- Kusiya ndi kutalikana nazo zotsutsana ndi kusala, chifukwa pali Hadith iyi:- Mtumiki anati:- "Kusala sikuleka kudya ndi kumwa kokha ai, koma kusala ndi kusiya zinthu zopanda phindu ndi kusiya kunena mau oipa. Tsono ngati wina atakutukwana kapena kukupanga zosayenera umuuzze kuti:- Ine ndasala ine ndasala."
- 6- Kufewa manja ndikuwerenga-werenga Qur'an. Ichi ndi chinthu chofunika kuchita nthawi ndi nthawi, koma makamaka mu Ramadhwan, chifukwa cha Hadith yomwe adailandira IBNU ABBAS (R.A) anati:- "Mtumiki (SAW) anali ofewa manja zedi kuposa anthu ena, ndipo nthawi imene amafewa kwambiri kuposa nthawi zonse ndi m'mwezi wa

Ramadhwan pamene amakumana ndi M'NGELO GABIR-IYERO, ndipo amakumana naye usiku uliwonse wa Ramadhwan, ndithu Mtumiki (SAW) amafewa manja zedi kuposa mphepo ya kum'banda kucha."

- 7- Pempho pa nthawi yomasula ndi mkati-kati mwa kusala chifukwa Mtumiki (SAW) anati:- "Ndithu munthu osala akamamasula ali ndi pempho losabwezedwa." Ndipo Mtumiki (SAW) pomasula anali kunena kuti:- "Mbuye wanga! Ndasala chifukwa cha inu, ndipo ndamasula pa chopereka chanu, kuyera konse ndi kwanu pamodzi ndi chiyamiko, mbuye wanga landirani kusala kwanga, inu ndinu akumva, odziwa."
- 8- Ngati uli mwezi wa Ramadhwan:- Kubindikira mu Mzikiti. Kubindikira ndiye kuti kukhala mu Mzikiti osatuluka popanda chifukwa chovomerezeka usiku ngakhale usana, ndikumangochulukitsa mapemphero ndi kuweringa Qur'an. Umboni wake ndi Hadith iyi:- "Mtumiki wa Mulungu anali kubindikira mu Mzikiti masiku khumi omaliza a mwezi wa Ramadhwan. Sanasiye zimenezo mpaka nthawi yomwalira inakwana iye akupangabe, kenaka anabindikira akazi ake."

M'malamulo a kubindikira ndi kubindikira mu Mzikiti womwe amapempheramo pagulu, ndipo asapange chom pangitsa kusamba, ndipo akhale ndi chitsimikizo cha kubindikira asanayambe, ndipo kumaonongeka chifukwa cha kutulukamo popanda chifukwa, ndi kutsimikiza kuti

atuluka, ngakhale asatuluke, ndi kukhudzana ndi mkazi, ndi kutulutsa madzi a chimuna. Mulungu wati:- "Ndipo musawakhudze akaziwo pamene inu mutabindikira mu Mzikiti." AL-BAQARA:187. Kubindikira sikuonongeka chifukwa chotuluka mu Mzikiti kukaimilira kapena kupanga chimbudzi, kapena kukasamba kuti akhale ndi "Twaraha" oyera, ndipo ngakhale atatuluka kukagula chakudya kapena chakumwa, koma asapite kukamuona munthu, ndipo asamapange mu Mzikitimo chinthu chosakhudzana ndi kubindikirako (ITIKAF)

- 9- Kumpatsa wina zoti adye pa kumasula kwake.
- 10- Kulimbikira kupanga zabwino kwa Mulungu, anthu ndi zinyama zomwe. Chifukwa ntchito yabwino m'mwezi wa Ramadhwan malipiro ake amakhala owonjezedwa kuposa myezi ina.
- 11- Kusunga mapemphero asanu pa tsiku:- Chifukwa anthu ambiri osala amagwa ulesi ndi mapemphero asanuwa, pamene mapempherowa ndi pamene pagona chipembedzochi, ndipo kuwasiya zimawerengedwa kuti ndi gulu la kutuluka m'Chisilamu.
- 12- Makhalidwe abwino:- Wonetsetsani kuti musapange zokutulutsani mu mpingowu ndipo musatukwane chipembedzochi, ndipo muwonetsetse kuti musakhale munthu wa makhalidwe oipa kwa anthu, chifukwa kusala kumayeretsa mtima, ndipo siiphunzitsa m'khalidwe woipa.

- 13- Phindulani nako kusala pokutenga ngati mpata wosiira kusuta fodya yemwe amayambitsa mabala a m'mimba (cancer), yetsetsani kuti mukhale amphamvu pofuna kuchita chinthu, musiye kusuta usiku monga m'mene mwasiira masana kuti mukhale a ngwiwo ndi wosunga chuma chanu.
- 14- Osadya mopitiriza muyezo pomasula, chifukwa mukatero muononga phindu la kusala ndipo musokoneza moyo wanu wangwiwo.
- 15- Chulukitsani kupereka zaulele kwa abale anu ndi ena aumphawi ndipo muyendere achibale anu ndi kuyanjanitsa odana.
- 16- Musacheze nthawi yaitali usiku chifukwa zingakulepheretseni kudzukira dakwi ndi pemphero la kum'mawa. Ndipo mukafuna kugwira ntchito mugwire molawilira kwambiri chifukwa Mtumiki (SAW) anati:- "Ambuyel Dalitsani anthu anga pa kulawilira kwawo."
- 17- Werengani mabuku onena zakusala kuti mudziwe kuti kudya ndi kumwa moiwala sikumasulitsa, ndipo kuziloterera kapena kudzuka mutakhudza mkazi wanu ndipo simunasambe sikumasulitsa, ngakhale kuti ndi koyenera kusamba usiku kuti mukhale oyera kuti mupemphere.

ZOSAFUNIKA PAKUSALA (بدء الصيام)

Pali zinthu zambiri zomwe anthu ambiri amachita pomwe akumanga zomwe ndi zosagwirizana ndi malamulo a chipembedzo chathu cha Chisilamu, kumachita kuti opangawo

amawerengera kuti ziri ndi malipiro abwino kwa Mulungu. Choncho tawona kuti ndi koyenera kuti tidziwitsane ndipo nazi:-

- 1- Sichoyenera kumanga mwezi wa Rajabu ndi Shabaan ndi cholinga chochingamira mwezi wa Ramadhwan koma chofunika ndi kusala m'myezi iwiri ndi cholinga chofuna kutsata zomwe Mtumiki wa Mulungu anali kuchita m'myeziyi. Chifukwa choti talamulidwa kutsatira zomwe amachita kuti tidzapeze malipiro abwino kwa chauta, iye (Mtumiki (MUPI) anali kuchulukitsa kusala m'myezi imeneyi. Umboni wa ndime imeneyi ndi mau ake a Mtumiki (MUPI). Mayi wa anthu okhulupilira mwa Mulungu Aisha chikondi cha Mulungu chikhale pa iye anati:-
 - (1) Anali Mtumiki wa Mulungu (MUPI) kusala masiku ochuluka m'mwezi wa Sha'baan kupatula masiku ochepepa okha (Idalandiridwa ndi Bukhariyy ndi Muslim)
 - (2) Ndi zosafunika kulankhula mokweza mau chitsimikizo cha kumanga (NIYAT) koma zofunika kuchita nkungotsimikiza pansi pa mtima wake munthu kuti mawa ndimanga (Insha Allah) chifukwa Mtumiki wa Mulungu (MUPI) anati "Malo a chitsimikizo ndi mu mtima ndipo kulankhula ndi pakamwa ndi zinthu zopeka, zolakwika [BID'AH]."
 - (3) Anthu ambiri akasala amachulukitsa kulavula chifukwa amakhala ndi chitsimikizo choti kumeza mate (malovu)

ndi kumasula. Izi ndi zolakwika chifukwa palibe kulakwa kulikonse ngati atameza, chifukwa malovuwo ali kale mthupi (mkamwa). Tsono zinthu zimene ziri mthupi kale sizimasulitsa kusala ai.

- (4) Monga tonsefe tikudziwa kuti cholinga chapamwambamwamba ndiponso choyambilira kumanga Ramadhwan chomwe Chauta watiuza ndi choti ife tiyenera kukhala omuopa Mulungu. Tsono pali anthu ena omwe Ramadhwan siimapindulira chirichonse, chifukwa choti amakhalabe akuchita chiwerewere, kumwa mowa ndi kusuta fodya komanso kusapemphera kasanu patsiku. Choncho zindikirani kuti palibe phindu lirilonse lomwe angapeze munthu yemwe satalikirana ndi zoterezi, ngakhale kuti zonsezi ndi zoletsedwa nthawi zonse koma mu Ramadhwan kunyansa kwake ndi koposa nthawi zina zonse.
- (5) Sikoyenera ndiponso ndikosabvomerezeka kwa munthu yemwe akumanga ndikumapita ku malo monga ku bar ngakhale kuti asakamweko mowa kapena kumvera nyimbo m'nyumba mwake ngakhalenso kwina kulikonse chifukwa Mulungu adaletsa.
- (6) Kusadekha pakupemphera pemphero la TARAWEH ndi kuwerenga AL-FATIHA ndi MASURATI ena mofulumira zomwe zichititsa kuti Marakat 21 apempheredwe mofulumira kwambiri, kumachita kuti zoterezi ndi zosayenera pa malamulo a chipembedzo.

- (7) i. Kuchedwetsa kumasula kumachita kuti malamulo ndi oti tiyenera kumasula mofulumira dzuwa likangotsimikizika kuti lalowa. Pomwe ambiri aife timadikira kupemphera kaye pemphero la Magarib komwe kuli kulakwitsa. Choncho zoyenera kuchita ndi zoti pomwe akuchita ADHANA ndi nthawi yomwe tiyenera kumwa madzi kapena chakudya chirichonse.

ii. Palinso anthu ena amene amadya DAKU (mfitsulo) mochedwetsa kwambiri kuchita kuthamangitsana ndi dzuwa, zoterezi ndi zolakwika chifukwa munthu amene angadye nthawi imeneyi ndiye kuti wamasula, choncho tiyenera kumayikira konzero kwambiri pa zinthu zofunikira ngati zimenezi. (Insha Allah).

(8) KUKONDWERERA USIKU WA AL QADR:-

(الإحتفال بليلة القدر)

Abale anga olemekezeka, kuti tilongosole za usiku umenewu, zonena ndi zambiri ndithu koma mwa chidule chomwe tingathe kufotokoza ndi choti:-

Usikuwu ndi opambana kwambiri tsono munthu ayenera kuchulukitsa kupempha Mulungu chikhululuko, kulapa machimo osiyana-siyana, kupempha zabwino za dziko lino lapansi ndi madalitso a tsiku lachiweruzo ndi zina zotero zomwe munthu amalakalaka ku mtima kwake. Nkhani idalandiridwa ndi IMAM BUKHARI yoti:- Mtu-miki (MUPI) likalowa dzuwa kapena kuti likakwana khumi lotsiriza la mwezi wa Ramadhwan anali kumanga

chilundu chake ndi kumakhala tsonga usiku kupemphera masiku khumi otsiriza aja ndiponso adali kuwadzutsa akunyumba kwake." Cholinga cha zonsezi ndi kuufufuza usiku wa mphamvu wa pamwamba (ALQADR).

Tsono zomwe timachita ambiri mwa ife mu usiku umenewu zimakhala zosemphana, zosiyana ndi njira yomwe Mtumiki (MUPI) adatiphunzitsa. Choncho tikafuna kuti tikhale anthu opindula ndi usikuwu tizichita mapemphero mwa njira yomwe tanena poyamba ija. Izitu munthu atha kuchita mu Mzikiti kapena kunyumba kwake ndipo ngati kuli ku Mzikiti ayenera kuchita payekha osati kusonkhana ndi kuchezera pakudya ndi kumwa ndi kuvina (ZIKIRI) ndi zopeka ziri kunja kwa Chipembedzo cha Chisilamu (BIDAH).

NB: Izi ndi zina mwa zinthu zomwe tidaona kuti ndi bwino kuti tidziwitsane mchipembedzo chathu cha Chisilamu zokhudzana ndi kusala kapena kuti kumanga m'mwezi wa Ramadhwan, ndipo ngati pali zina zomwe tayiwala kapena kulakwitsa tikukupemphani kuti mutidziwitse kupyolera m'makalata kapena phone (Insha Allah).

MULUNGU ATIKHULULUKIRE PA ZOLAKWA
ZATHU POTI IYE NDI AMENE ALI NDI CHIFUN-
DO CHOPOSA ALIYENSE.